



M'busa Alamo

Osatenga Konse Lembala Chilembo apo ayi Mudzakhumudwa kwa Muyaya

Olemba Tony Alamo

Mu chaputara cha 24 cha Mateyu, ophunzira a YESU anamufunsa IYE nati mutiuze ife dziko lidzatha liti ndipo chizindikiro cha kufika KWAKE nchiani (Mateyu 24:3). Lamulo lofunika kwambiri komanso chizindikiro chofunika kwambiri chakudza KWAKE padziko lapansi ndi kukhala tcheru ndi aneneri onyenga, kuti asakusokeretseni. Chizindikiro ichi ndichofunika kwambiri ndipo YESU anachitchula poyambilira pa zizindikiro zonse (Mateyu 24:4). IYE anati, “Samalirani kuti asasokeretse inu munthu. Pakuti ambiri adzadza m'dzina LANGA, nadzanena, Ine ndine KHRISTU; nadzasokeretsa anthu ambiri” (Mateyu 24:4-5).

Wokana Khristu adzati iye ndi KHRISTU, nadzasokeretsa ambiri.¹ YESU anachenjeza za izi kokwana kasanu yekha mu Mateyu chaputara 24, chifukwa Satana ndi wonyenga

kwambiri kotero kuti ananyenga dziko lonse.² Kenako Yesu ananena za nkondo ndi mphekesera za nkondo, za mtundu kuukirana ndi mtundu wina ndiponso ufumu kuukirana ndi ufumu wina, njala, milili, ndi zivomezi kulikonse (Mateyu 24: 6-8).

“Pomwepo iwo [mphamvu yoyipa yadziko yachinayi ndi yotsiriza³] adzakuperekani inu kwa chisautso, ndipo adzakuphani inu [kuna kuti akuchita utumiki wa MULUNGU pakupha mwadala Akhristu obadwanso mwatsopano⁴]: ndipo inu mudzadedwa ndi mafuko onse chifukwa cha dzina LANGA. [Dzina la YESU ndi MAWU a MULUNGU⁵—ndipo mudzadedwa chifukwa cha kulalikirira MAWU AKE.] Ndiyeno [chifukwa cha chizunzo choopsa] ambiri adzakhumudwa, nadzaperékana wina ndi mzake, nadzadana wina ndi mzake” (Mateyu 24: 9-10).

“Ndipo aneneri onama ambiri adzauka, nadzasokeretsa anthu ambiri” (Mateyu 24:11). YESU, kachiwiri, anachenjeza za aneneri onyenga. Vesi 12 imanena kuti mudzakhala uchimo wambiri m'dziko lonse mwakuti “chikondi cha ambiri chidzazilala.” Mu vesi 13, YESU akulonjeza anthu enafe amene tidzapirire mpaka pa mapeto, yemweyo adzapulumuka. Koma ambiri amene anapulumutsidwa sadzapirira, kotero iwo sadzapulumuka.⁶ Iwo adzagwa. “Ndipo uthenga uwu wabwino wa ufumu udzalalikidwa m'dziko lonse lapansi kuti ukhale umboni ku mitundu yonse; ndipo pomwepo chidzafika chimaliziro. Pamene inu kotero mudzawona chonyansa cha kupululutsa, chimene chidanenedwa ndi Danieli mneneri, chitaima m'malo oyera [kutanthauza kukhala mu

(Yapitirira patsamba 2)

1 Dan. 11:21-45, 2 Ates. 2:3-4, Chiv. chap. 13 2 Gen. 3:1-6, Mat. 24:4-5, 11, 23-27, Yoh. 8:44, 2 Akor. 11:13-15, 2 Ates. 2:3-12, Chiv. 2:9, 12:9, chap. 13, 16:13-14, 17:8, 18:23, 19:19-21, 20:1-3, 7-8 3 Dan. 2:40, 7:19-25, 8:16-26, Chiv. 13:1-8, chap. 17 4 Yoh. 16:2 5 Yoh. 1:1, 14, Chiv. 19:13 6 Ezek. 33:12-13, Mat. 5:13, 12:43-45, 24:45-51, Luka 9:62, Yoh. 15:6, Aro.11:22, Akol. 1:21-23, 2 Ates. 2:3, 1 Tim. 1:19, 2 Tim. 2:12, Aheb. 3:6-19,4:1-11, 6:4-8, 10:25-31, 38-39, 2 Pet. 2:20-22, 1 Yoh. 3:6-10, 2 Yoh. 9, Yuda 5-6, Chiv. 2:4-5, 3:2-3

Osatenga Konse Lemba la Chilembo apo ayi Mudzakhumudwa kwa Muyaya

(Yachokera patsamba 1)

MZIMU kusunga malamulo A YEHOVA⁷]” (Mateyu 24: 14-15).

“Pakuti pomwepo padzakhala masauko akuru, monga sipadakhale otero kuyambira chiyambi cha dziko, iai, ndipo sipadzakhalanso. Ndipo akadaleka kufupikitsidwa masiku awo, sakadapulumuka munthu ali yense: koma chifukwa cha osankhidwawo masiku awo adzafupikitsidwa. Pomwepo munthu akanena kwa inu, Onani, Khristu ali kuno, kapena uko; musamuvomereze” (Mateyu 24:21-23).

Anabwerenza, YESU kunena za Akhristu wonyenga ndi aneneri wonyenga. Ichi ndi chifukwa ngati inu

mukukhulupirira iwo, mudzakhala muyaya mu Gehena mu Nyanja ya Moto.⁸ Aneneri opanda umulungu a boma lonyenga la usatanali adzakuuzani kuti ngati mutenga chilemba cha chirombo, iwo adzakumasulani m’ndende, ngakhale muli zilango zokhala m’ndende nthawi yaitali. Iwo adzakupatsani ntchito za m’boma, zimene zidzakupulumutseni inu kupereka misonkho yambiri. Simudzakhala ndi vuto kupeza chakudya kapena kulipira chili chonse—mungogwadi- ra Chirombo (malamulo a boma la dziko). Tengani chilemba chake, ndipo simudzazunzika. Mudzatha kugula ndi kugulitsa; koma kumbukirani, ngati mutenga chilemba, mudzakhala mwachitira mwano MZIMU WOYERA, ndipo palibe chikhululukiro cha tchimo loipa ili.⁹

“Chifukwa chake akanena kwa inu, Onani, IYE ali m’chipululu; musamukeko: onani, IYE ali

m’zipinda; musabvomereze” (Mateyu 24:26). Apanso YESU akutichenjeza tonse zokhudza aneneri onyenga. Chifukwa cha zozizwitsa zopangidwa ndi munthu, iwo adzanyenga osankhidwawo.¹⁰ YESU akutiuzza mmene tidzadziwire akadzakhaladi IYE: “Pakuti monga mphezi idzera kum’wawa, nionekera kuwala kufikira kumadzulo; kotero kudzakhalanso kufika kwake kwa MWANA wa MUNTHU” (Mateyu 24:27). “Pakuti kuli konse uli mtembo, ziombankhanga zidzasonkhanira konko. [Chiombankhanga ndi chim’dya nyansi, ngati chipungu. Pamene mpingo waonongeka ndi mabodza, Satana adzakhala kumeneko. Satana amachita izo, ndipo anthu a mpingo ndikukhulupirira.]

“Koma pomwepo atangotha masauko a masiku amenewo dzuwa lidzadetsedwa, ndipo mwezi sudzasonetsa kuwala kwake, ndi nyenyezi

7 Ezek. 11:19-20, 36:26-27, Yoh. 3:4, Aro. 8:1-14, Agal. 5:16-18, 25 8 2 Pet. 2:1-3, 1 Yoh. 4:1, Chiv. 19:20, 20:10-15, 21:8 9 Mat. 12:31-32, Chiv. 14:9-11, 20:4 10 Marko 13:22, 2 Ates. 2:8-10, Chiv. 13:11-15, 16:12-14, 19:20

Makalata opita kwa M’busa Alamo

New York

Okondeka M’busa wa Dziko Alamo,

Ndinakumanizana ndi kope lanu la nkhani za m’makalata za dziko la pansi ndipo ndinachita nalo chidwi. Mawu oti “Ozerezeka” m’malembo akuluakulu unandipatsa chidwi. Zithunzi za Hitler, Obama ndi Papa ndithu zinandifikapo!! Ndimaona mizukwa yoyendayenda usiku yokumwa magazi imeneyi ikuyamwa magazi a wanthu osowa thandizo ndi osazindikira. Ayiwala Mulungu wathu ndi ntchito zabwino zomwe lye wachita ndipo adzalipira!!!

Sine mulendo kwa anthu amtundu wotere; Ine makamaka ndimagwira ntchito mogwirizana ndi miyoyo yotayikayi yomwe ndimakhulupirira kuti ikudikirira kupezedwa.

Nditawerenga imodzi mwa makalata a nkhani zanu, ndikukhulupirira kuti ndinu osankhidwayo odzayatsa ndikuthandiza maganizo omwe ali mwa ambiri mwa ife.

Mwa ulemu ndikupempha mundiyikeko pa ndandanda wa olandila nkhani zanu za m’makalata. Ndizotsitsimutsa kwambiri kukhuthulidwa ndi mau achilungamo.

Mulungu akudalitseni inu M’busa wa dziko ndipo ndikukuthokozani pokhutula kuti sine ndekha amene ndili ndi maganizo amenewa pa dziko la pansi pano.

Modzipereka,
Dom Carpentieri

Floral Park, NY

India



Rev. D.R. Moses kugawa zolembe za Uthenga Wabwino za M’busa Alamo m’midzi ya Andhra Pradesh, India

Ndili okondwa kwambiri chifukwa chogawa zolembe za M’busa Alamo m’tchalichi mwathu ndi kwa mitundu ya anthu, yomwe imalandila zotanthauzilidwa mu chi Telugu. Ngati nkothe- ka mutitumizile zolembe za m’chi Telugu, chifukwa tonse ndife abusa ndi achinyamata. Ndikukuthokozani Abusa, Wanu mu ntchito Zake, Rev.D.R.Moses, Voice of Zion Prayer House Andra Pradesh, South India

zidzagwa kuchokera kumwamba, ndi mphamvu za kumwamba zidzagwedezeka: Ndipo pomwepo [osati chisanachitike, koma pomwepo—nthawi yomweyo CHITANGOTHA chisautso] mudzaoneka chizindikiro cha MWANA wa MUNTHU m'mwamba: ndipo mitundu yonse ya pa dziko lapansi idzadziguguda pachifuwa, nidzapenya MWANA wa MUNTHU alinkudza m'mitambo ya kumwamba ndi mphamvu ndi ulemereero waukulu. Ndipo IYE adzatumiza angelo AKE ndi kulira kwakukulu kwa lipenga, ndipo iwo adzasonkhanitsa osankhidwa AKE ku mphepo zinai, kuyambira malekezero a kumwamba kufikira malekezero ake ena” (Mateyu 24:28-31).

Tsopano YEHOVA anauza Satana ndi ife tonse kuti munthu sadzakhalala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi MAWU onse akuturuka m'kamwa mwa MULUNGU (Mateyu 4:4). Choncho, sitikuyenera kulola maulosi a chisautso chachikulu mu Mateyu chaputala 24, Danieli chaputala 7, ndi bukhu la Chivumbulutso kutipatsa mantha nkupita m'manja mwa Satana, koma ife moyo wathu ukhalire mwa MAWU a MULUNGU onse, monga Salimo 37: “Usabvutike mtima chifukwa cha ochita zoipa, usachite nsanje chifukwa cha ochita chosalungama. Pakuti adzawamweta msanga monga udzu, ndipo adzafota monga msipu wauwisi. Khulupirira YEHOVA, ndipo chita chokoma; khala m'dziko, ndipo udzadyetsedwa ndithu. Udzikondweretsenso mwa YEHOVA; Ndipo IYE adzakupatsa zokhumba mtima wako. Perekana njira yako kwa YEHOVA; Khulupiriranso mwa IYE; ndipo IYE adzachichita. Ndipo IYE adzaonetsa chilungamo chako monga kuunika, ndi kuweruza kwako

monga usana. Khala chete mwa YEHOVA, numlindirire IYE: Usabvutike mtima chifukwa cha iye wolemerera m'njira yake, chifukwa cha munthu amene abweretsa zipangizo zoipa kuti zichitike. Leka kupsa mtima, nutaye mkwiyo: usabvutike mtima ungachite choipa. Pakuti ochita zoipa adzadulidwa: koma iwo akuyembekeza YEHOVA, iwowa adzalandira dziko lapansi.

“Kwatsala nthawi yochepe, ndipo woipa adzatha psiti: Inde, udzayang'anira mbuto yake, nudzapeza palibe. Koma ofatsa adzalandira dziko lapansi; nadzakondwera nao mtendere wochulukana. Woipa apanzira chiwembu wolungama, namkukutira mano. AMBUYE adzamseka: popeza IYE apenya kuti tsiku lake likudza. Oipa asolola lupanga, ndipo akoka uta wao, kuti alikhe ozunzika ndi aumphawi, ndikupha amene ali oongoka m'njira. Lupanga lao lidzallowa m'mtima mwao momwe, ndipo mauta ao adzathyoledwa.

“Zochepe zake za wolungama zikoma koposa chuma chochulukana cha oipa ambiri. Pakuti manja a oipa adzathyoledwa: Koma AMBUYE achirikiza olungama. AMBUYE adziwa masiku a anthu angwiro: ndipo chowasiyira chao chidzakhalala chosatha. Sadzachita manyazi m'nyengo yoipa: ndipo m'masiku a njala adzakhuta. Koma oipa adzatha, ndipo adani ake a YEHOVA adzakhala ngati mafuta a ana a nkhoza: adzanyeka; mu utsi adzakanganuka. Woipa akongola, wosabwezanso: koma wolungama achita chifundo, napereka. Pakuti iwo amene IYE awadalitsa adzalandira dziko lapansi; ndipo iwo amene IYE awatemberera adzadulidwa.

“YEHOVA akhazikitsa mayendwedwe a munthu wabwino: ndipo akondwera nayo njira YAKE. Angakhale akagwa, satayikiratu: pakuti YEHOVA am'gwira ndi dzanja LAKE. Ndinali mwana, ndipo ndakalamba; koma sindinapenye wolungama wosiyidwa, kapena mbumba

zake zili nkupempha chakudya. Tsi-ku lonse achitira chifundo, nakon- goletsa; ndipo mbumba zake zidalit- sidwa. Siyana nacho choipa, nuchite chokoma; nukhale nthawi zonse. Pakuti YEHOVA akonda chiweruzo, ndipo sataya anthu AKE oyera mitima; asungika kosatha: koma adzadula mbumba za oipa. Olungama adzalandira dziko lapansi, nadzakhalala momwemo kosatha. Pakamwa pa wolungama palankhula zanzeru, ndi lilime lake linena chiweruzo. Malamulo a MULUNGU wake ali mumtima mwake; pakuyenda pake sadzaterereka. Woipa aunguza wolungama, nafuna kumupha. YEHOVA sadzamusiya m'dzanja lake, ndipo sadzamutsutsa poweruzidwa iye.

“Yembekezera pa YEHOVA, nusunge njira YAKE, ndipo IYE adzakukweza kuti ulandire dziko: Pakudulidwa oipa, udzapenya. Ndapenya woipa ali muudindo waukulu, natasa monga mtengo wauwisi wanzika. Koma anafa, ndipo, taona, kwati zi: inde, ndipo ndinayesa kumufunafuna, koma osampeza. Tapenya wangwiro, ndipo taona woongoka mtima: pakuti ku matsiriziro ake a munthuyo kuli mtendere. Koma olakwa adzaonongeka pamodzi: matsiriziro a oipa adzadulidwa. Koma chipulumutso cha olungama chidzera kwa YEHOVA: IYE ndiye mphamvu yao m'nyengo ya nsautso. Ndipo YEHOVA awathandiza, nawalanditsa: awalanditsa kwa oipa, nawapulumut- sa, chifukwa kuti anamukhulupirira IYE” (Masalimo 37).

Mapeto odziwira “zinsinsi zakuya za Satana, monga anenera” ndi chiro-ombo (boma la dziko) ndi chilembo cha chiroombo (Chivumbulutso 2:24). Aliyense amene achimwa mwadala sangalowe Kumwamba.¹¹ (Chivumbulutso 14:9-11). Werengani ndi kuphunzira MAWU a MULUNGU.¹² Udindo wonse wa munthu ndi “kuopa MULUNGU, ndi kusunga malamulo AKE” (Mlaliki 12:13).

(Yapitirira patsamba 4)



¹¹ Mat. 12:31-32, Yoh. 5:14, 8:11, Aheb. 6:4-8, 10:26-31, 2 Pet. 2:20-22, Yuda 5-6 ¹² Aro. 15:4, 2 Tim. 2:15, 3:14-17

Osatenga Konse Lemba la Chilembo apo ayi Mudzakhumudwa kwa Muyaya

(Yachokera patsamba 3)

Vomerezani AMBUYE YESU KHRISTU pakunena pemphero ili, ndipo mudzapulumuka (Machitidwe 16:31):

AMBUYE wanga komanso MULUNGU wanga, ndichitireni chifundo ndine munthu wochimwa.¹³ Ndikukhulupirira kuti YESU KHRISTU ndi MWANA wa MULUNGU wamoyo.¹⁴ Ndimakhulupiranso kuti IYE anafera pamtanda ndipo anakhetsa mwazi WAKE wantengo wapatali ndi cholinga choti machimo anga onse akhululukidwe.¹⁵ Ndikukhulupiranso kuti MULUNGU anaukitsa YESU kwa akufa pogwiritsa ntchito mphamvu ya MZIMU WOYERA,¹⁶ ndiponso kuti IYE anakhala kudzanja lamanja la MULUNGU ndipo panopa akumva pemphero langa lolapali.¹⁷ Ndikutsegula zitseko za mtima wanga, ndipo ndikukuyitanani kuti mulowe mumtima mwanga, inu AMBUYE YESU.¹⁸ Tsukani machimo anga ambirimbiro achoke onse mu mwazi wantengo wapatali umene INU munakhetsa m'malo mwanga pamtanda wa ku Kavari.¹⁹ Ndikudziwa

kuti mundimvera pemphero langali AMBUYE YESU; INU mukhululukira machimo anga ndi kupulumutsa moyo wanga. Ndikudziwa izi chifukwa MAWU ANU, Baibulo, limanena zimenezi.²⁰ MAWU ANU amati INUYO simudzakana kumvetsera pemphero la munthu aliyense, ndipo ine ndili m'gulu la anthu amenewo.²¹ Choncho, ndikudziwa kuti INUYO mukundimvetsera pamene ndikupemphera ndipo ndikudziwanso kuti INUYO mundiyankha komanso mudipulumutsa.²² Ndipo ndikukuthokozani AMBUYE YESU, chifukwa chopulumutsa moyo wanga, ndipo ndisonyeza kuyamikira mwa kuchita zinthu zimene INUYO munalamula komanso kupewa kuchita uchimo.²³

Pambuyo pa chipulumutso, YESU ananena kuti munthu ayenera kubatizidwa pomizidwa thupi lonse m'madzi, m'dzina la ATATE, ndi la MWANA, ndi la MZIMU WOYERA.²⁴ Muziphunzira mwakhama Baibulo la *Buku Lopatulika Ndilo Mau a Mulungu*, [King James Version] ndipo muzichita zimene Baibulolo limanena.²⁵

AMBUYE akufuna kuti inuyo muziwuza ena za chipulumutso chanu. Mungathe kukhala wofalitsa uthenga wabwino wa M'busa Tony Alamo. Tizikutumizirani mabuku mwaulere. Imbani foni kapena tumizani imelo kwa

ife kuti mudziwe zambiri. Tikukupemphani kuti muwuzeko ena uthengawu.

Ngati mukufuna kuti dziko lipulumutsidwe monga m'mene YESU akulamulira, mukufunika kupereka chakhumi kwa MULUNGU. MULUNGU anati, "Kodi munthu angabere MULUNGU? Inde, mwandibera kale. Koma akuti, Ife tikumubera bwanji MULUNGU? Mu chakhumi ndi mu zopereka. Anthuwo ndi otembereredwa chifukwa akundibera, ngakhale mtundu wonsewu [dziko lonse lapansi]. Bweretsani nonse chakhumi ['chakhumi' ndi gawo limodzi la magawo khumi (10%) ya malipiro anu] m'nkhokwe zanga n'cholinga choti pakhale nyama [chakudya cha Uzimu] mu nyumba YANGA [anthu opulumutsidwa] kuti mudiye, akutero AMBUYE wa MAKAMU, kuti muone ngati sindizakutsegulirani mazenera a Kumwamba ndi kukukhuthulirani madalitso amene mudzasowa malo owalandirira." Ndipo ndizadzudzula anthu okudyerani masuku pamutu ndipo sadzawononga zipatso za nthaka yanu; ngakhale m'phesa wanu sudzalephera kubala zipatso pa nyengo yake m'minda yanu, watero AMBUYE wa MAKAMU. Ndipo mitundu yonse idzakutchani odala: chifukwa dziko lanu lidzakhala labwino, watero AMBUYE wa MAKAMU" (Malaki 3:8-12).

13 Sal. 51:5, Aro. 3:10-12, 23 14 Mat. 26:63-64, 27:54, Luka 1:30-33, Yoh. 9:35-37, Aro. 1:3-4 15 Mac. 4:12, 20:28, Aro. 3:25, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 5:9 16 Sal. 16:9-10, Mat. 28:5-7, Marko 16:9, 12, 14, Yoh. 2:19, 21, 10:17-18, 11:25, Mac. 2:24, 3:15, Aro. 8:11, 1 Akor. 15:3-7 17 Luka 22:69, Mac. 2:25-36, Aheb. 10:12-13 18 1 Akor. 3:16, Chiv. 3:20 19 Aef. 2:13-22, Aheb. 9:22, 13:12, 20-21, 1 Yoh. 1:7, Chiv. 1:5, 7:14 20 Mat. 26:28, Mac. 2:21, 4:12, Aef. 1:7, Akol. 1:14 21 Mat. 21:22, Yoh. 6:35, 37-40, Aro. 10:13 22 Aheb. 11:6 23 Yoh. 5:14, 8:11, Aro. 6:4, 1 Akor. 15:10, Chiv. 7:14, 22:14 24 Mat. 28:18-20, Yoh. 3:5, Mac. 2:38, 19:3-5 25 Deut. 4:29, 13:4, 26:16, Yos. 1:8, 22:5, 2 Tim. 2:15, 3:14-17, Yak. 1:22-25, Chiv. 3:18

Ngati mukufuna kudziwa zambiri kapena ngati mukufuna mabuku kapenanso nkhani zina zimene zimakusangalatsani, tiimbireni foni kapena tilembereni.

Tony Alamo, World Pastor, Tony Alamo Christian Ministries Worldwide • P.O. Box 2948, Hollywood, CA 90078

Lamya ya pemphero ndi uthenga maola 24: +1 (661) 252-5686 • Fax +1 (661) 252-4362

www.alamoministries.com • info@alamoministries.com

Tony Alamo Christian Ministries Worldwide imalandira anthu onse ndipo imapereka zinthu zofunika kwa onse amene ali ku U.S. amene akufunitsitsadi kuti ayambe kutumikira AMBUYE ndi mtima wawo wonse moyo wawo wonse ndi mphamvu zawo zonse

Mapemphero amachitika usiku uli wonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi Lamulungu nthawi ya 3 Koloko madzulo ndiponso

8 Koloko usiku ku Tchalitchi cha kudera la Los Angeles: 13136 Sierra Hwy., Santa Clarita, CA 91390, +1 (661) 251-9424

Magalimoto a ulere opita ndi kuchokera ku mapemphero amaperekedwa pa kona ya Hollywood Blvd. ndi Highland Ave.,

Hollywood, CA tsiku lili lonse nthawi ya 6:30 madzulo, Lamulungu lili lonse nthawi ya 1:30 madzulo ndi 6:30 usiku.

Mapemphero amachitika mu Mzinda wa New York Lachiwiri lili lonse nthawi ya 8 Koloko usiku ndi madera ena usiku okhaokha. Chonde

imbani foni kuti mumve zambiri: +1 (908) 937-5723. ZAKUDYA ZIMAGAWIDWA PA MAPETO PA MAPEMPHERO ALI WONSE

Funsani buku la M'busa Alamo, lakuti Mesiya, losonyeza KHRISTU kuyambira ku Chipangano Chakale mu maulosi oposa 333.

Khalani wogwira ntchito yokolola miyoyo ya anthu pakukhala ogawira mabuku a M'busa Alamo

Mabuku ndi zinthu zonse zomvetsera n'zaulere, ndipo simulipira ndalama yotumizira

Ngati wina akukuuzani kuti mupereke ndalama pa zinthu zimenezi, chonde imbani pa +1(661) 252-5686.

M'BUKU ILI MULI CHIKONZERO CHENICHENI CHA CHIPULUMUTSO (Machitidwe 4:12).

MUSALITAYE, PATSANI ENA KUTI AWERENGE.

Anthu amene muli m'mayiko ena, tikukulimbikitsani kuti mumasulire n'chinenero chanu mabukuwa. Ngati

mukusindikizanso bukuli, musaiwale kuika mawu ali m'munsiwa omwe ndi okhudzana ndi zamalamulo:

© Copyright June 2012, 2015 All rights reserved World Pastor Tony Alamo © Registered June 2012, 2015
CHICHEWA/NYANJA—VOLUME 16100—NEVER TAKE THE MARK OF THE BEAST OR YOU WILL BE ETERNALLY SORRY